

# Kuthandizira Mwana Wanu Kudziwa za Maphunziro a Ana a Chichepere ndi Ntchito za Kusamalira.

**NYANJA/CHEWA**

Kuyamba bwino pa maphunziro a ana achichepere ndi kofunika ndithu. Ndikofunikira kuti inu ndi banja lanu mukumva kuti mwalandiridwadi, ndinu wotetezedwa komanso wothandizidwa. Masiku woyamba a pamalo athandizo ndi kuti mwana wanu adziwe ana ena ndi kuyamba kudalira ubalewo ndi aphunzitsi awo, ndi ena wogwira ntchito pakati pa ana achichepere.

Maphunziro a Ana a Chichepere ndi Ntchito za Kusamalira mu Victoria zimatsogozedwa ndi chigawo cha *Victorian Early Years Learning and Development Framework* (VEYLDF). Dongosolo limeneli limathandiza aphunzitsi kuti kudziwa ana ndi mabanja awo ndi mbiri ya chikhalidwe chawo ndipo zimathandiza pa maphunziro awo. Ana amamva kulandiridwa ndipo amaphunzira bwino kwambiri pamene akatswiri a ntchito amapereka ulemu ndi kuzindikira m'mene anawo alili (VEYLDF, 2016, tsamba 12). Kumvetsaku kudzathandiza njira imene aphunzitsi amagwiritsa ntchito pothandiza inu ndi mwana wanu pa nthawi yoyambirira komanso kukhazikika poyamba kwa maphunziro awo atsopano a Maphunziro a Ana a Chichepere ndi Ntchito za Kusamalira.

Maphunziro a Ana a Chichepere ndi Ntchito za Kusamalira zimaona pa mgwirizano pakati pa ophunzitsa ndi mabanja kukhala maziko a dongosolo lodalirika ndi labwino. Ulemu wa ubale wochokera pa chiyambi ndi chizindikiro cha ntchito yabwino yakusamalira. Mutha kuyembekezera ophunzitsa kukhala wokoma mtima komanso wosangalala pakukulandirani ndi kukulimbikitsani kugwiritsa ntchito chilankhulo kapena zilankhulo za banja lanu.

Zisamaliro zitha kuchitika mwa kupyolera pa foni pokhala wina womasulira chilankhulo kuonetsetsa kuti zonse zikumveka momwe ziyenera kukhalira ndi kupereka danga la kufunsa mafunso ndi kufunsa zina m'chilankhulo chomwe mungamasuke nacho kwambiri inuyo. Kuonjezera apo, wantchito wothandiza amene amalankhula chilankhulo cha banja lanulo akhoza kupezekapo ndi kuthandizira mwana wanu kwa nthawi yochepa pomwe mwanayo akuyesetsa kukhazikika ndi kuzindikira za malowo ndi zithandizo zopezekapo.

Maphunziro abwino kwambiri amazindikira kuti mabanja ndiwo maziko enieni amaphunziro a ana ndi kukula kwa iwo (VEYLDF, 2016, tsamba 9). Ophunzitsa amalemekeza ndi kupempha thandizo la banja pa ndondomeko ya zaka zoyambirira za ana. Zimenezi sizithandiza chabe machitidwe a ophunzitsa komanso zimathandiza ana kukhala ndi kulimbitsa chidaliro, chitetezo ndi kulumikizana pakati pa anthu mu maphunziro awo ndi kusamalira malo ozungulira ndi zochitika ku makomo kwawo zimene zithandiza koposa zotulukamo za maphunziro. Mabanja nawonso amalimbikitsidwa kutengako mbali pa kusamalira ndi kukhalapo pa nthawi zoyambirira. Zimenezi zimathandiza mwana wanu kumva kuti ali wotetezeka ndipo zimathandizanso inuyo kumvetsa zomwe zimachitika pa malowa pomwe mwana wanu amakhala inuyo mutachoka.

Malo a ana a chichepere amakhala ndi dongosolo la chisamaliro kuthandizira inuyo ndi mwana wanu kudziwa ndi kuzolowera zisamaliro zomwe zilipo. Zina zopezekapo ndi;

- kuyendera malowo ndi mwana wanu pomwe maphunziro asanayambe
- kuyamba ndi kukumana kwa nthawi yochepa chabe ndi kumakulitsa nthawiyo pothandiza inu ndi mwana wanu kukhala aufulu.

Aphunzitsi anu a ana a chichepere adzakhala ndi nthawi ya kukambirana ndi inu ndi kukufunsani mafunso okhudza inu komanso mwana wanu. Ichi chidzawathandiza kumvetsa zofuna za mwana wanu ndi kuwathandizanso kupanga pulogalamu yothandiza pakuphunzira kwa mwanayo kuti yikhale ndi zotulukamo zomuyenerera.

Zitsanzo za zina zimene mungathe kufunsidwa za pamalo a kusamalirapo ana a chichepere ndi monga mfundo zotere;

- Mfundo zokhudza ndi umoyo wa mwana – zipepala za katemera, mankhwala angafunikire, matenda kapena zosamuyanja mwanayo.
- M'mene amakondera kusintha matewera, m'mene amakondera kuchita chimbuzi ndi zimene amazolowera kuchita ku nyumba.
- Zakudya zimene ana amadya, nthawi imene amadyerapo.
- Kupuma kwa mwana / zofunika pogona.
  - Kodi amagona mu chifukwato, kapena pa kama wawo kapena amagona ndi wina?
  - Kodi ndi nyimbo zotani zimene zingawamvetse bwino?
  - Kodi ali ndi buku imene amakonda kwambiri, kapena chidoli chapadera, kapena gombeza?
  - Kodi ndi nthawi yanji imene amakonda kupuma/kugona m'masana?
- Kodi ndi zisangalalo kapena zachikhalidwe zotani zimene ndizofunikira ku banja lanu?
- Aphunzitsi adzakondwera kulandira mfundo zina zimene mungakonde kugawana nawo.
- Mudzakhalanso ndi mfundo zanu zokhudza mwana zimene mudzafuna kuti ophunzitsa adziwe kuti ziwathandize pakuthandiza mwana wanu.

## Njira zina zothandiziramo mwana wanu pamene akukhazikika ndi kulandira chisamaliro cha pa malo a ana a chichepere

- Pezani nthawi yakukhala ndi mwana wanu pa malopo – fotokozerani mwanayo za zochitita mobwerezabwereza, sewerani naye, werengani nkhani ndi kuyimba nyimbo za m'chilankhulo chanu.
- Athandizeni kulankhulana ndi ana anzawo. Monga mwakungokhala pafupi ndi anzake, kuzidziwitsa nokha kwa ana ena, kulowelerapo pomwe achita zochitika ndi kuchita nawo masewera.
- Khalani ndi nthawi ya kulankhulana ndi mwana wanu ndi ena amene amalankhula chilankhulo chofanana ndi chanu.
- Lankhulani nawo ana anu pa zomwe akumvera ndi kupitamo: atsimikizireni ndi kuwalimbikitsa.
- Onetsetsani kuti mwana wanu awadziwa aphunzitsi ake, maina awo ndikuti akukhoza kupita kwa iwo ngati akufuna thandizo. Apatseni m'pata wakunena mobwerezabwereza maina a aphunzitsi awo ndi inu nomwe ndipo muyese kuchita sewero la kupempha thandizo.
- Nthawi zonse muuzeni kuti mwapita musanachoke ndipo mutsimikizireni kuti mudzabweranso bwino lake. Ndi ganizo labwino kuona kuti mwana wanu wakhazikika pakumuthandiza kuchita chochitika pamodzi ndi womuphunzitsa kapena pamodzi ndi ana ena musanachoke pamalo amenewo.
- Kambiranani za zochitika komanso za malo amenewo ndi ana pa nthawi ya usiku komanso m'mawa asanapite kuti muwapatse m'pata wakufunsa mafunso komanso kuti inu muyankhepo ngati pali nkhawa ina iliyonse imene akhoza kukhala nayo.
- Kumbukirani kuti ophunzitsa mwana wanu aliko kuti athandizire inu ndi mwana wanu pa nthawi yanu yakukhala pa malo amenewo.

---

**Maumboni**

Department of Education and Training, 2016. *Victorian Early Years Learning and Development Framework*.